**REPUBLIC OF MALAWI**

# SPEECH

**BY HIS EXCELLENCY**
**DR. LAZARUS McCARTHY CHAKWERA**
**PRESIDENT OF THE REPUBLIC OF MALAWI**

**ON INDEPENDENCE DAY**

**BINGU NATIONAL STADIUM**
**LILONGWE, MALAWI**
**SUNDAY, 6TH JULY 2025**

**Amayi ndi Abambo,**

**Mutati mufunse ma biludala onse mdziko muno, atha kukuuzani kuti ntchito yomanga maziko siifunika kuigwira mwa phuma kapena mwachidule. Kumanga maziko mwa phuma ndi chiyambi changozi, chifukwa nyumba yopanda maziko olimba siichedwa kugwetsedwa ndi mphepo kapena ndi katundu wolemetsa. Olo stadium inoyo kuti tonse tikhalemo mwaunyinji chonci popanda chiopsyezo, ndi chifukwa choti omangawo anadzala maziko amphamvu mwachifatse ndi mwaukatswiri. Ndiye lero pamene tikulingalira zomanga maziko atsopano adziko lathu, kapena pamene tikulingalira zomanganso maziko omwe anaonongeka mdziko muno, tisayembekeze kuti ntchito yake ndi ya chidule ayi.**

**Komano chofunikira ndi choti tonsefe ntchitoyo tiimvetsetse, chifukwa tikamakamba zomanga maziko atsopano adziko lathu, tonse tikhale ndi chiganizo chimodzi pozindikira kuti maziko tikuyenera kumangawo ndi atiwo.**

**Ndiye ine ndinena maganizo anga, kuti nanunso muganizire mbali yomwe mukuiona kuti ndiyofunikira.**

**Poyambilira penipeni, sitingamange dziko latsopano ngati sitikhazikitsa maziko a chikhalidwe. Dziko la anthu otaya chikhalidwe chawo kapena la anthu osasunga chikhalidwe chawo limavuta kutukula. Ndichifukwa chake olo timange miseu kapena zitukuko zina, sichingakhalitse ngati anthu opanda khalidwe azibwela nkumaphwasula kuti atengemo njerwa ndi zitsulo kuti akagulitse. Olo tigule mankhwala nkukaika mchipatala, ngati khalidwe lokuba mankhwalawo kuti wina akagulitse silithetsedwa mdziko muno, mavuto osowa mankhwala saazatha. Ndiye maziko oyamba kumanga mdziko muno akhale chikhalidwe. Munthu amene tikumuona kuti ali ndikhalidwe loononga sitiyenera kumusekelera. Komano masiku ano ambiri ayife anthu omwe ali ndi khalidwe loononga timawadziwa, koma timangoyang'anira ngati kuti sitikuona. Kusekelera munthu wakhalidwe loononga kuti apitirize kuononga ndi chinthu chimodzi chomwe chaononga maziko adziko lino.**

**Dziko lanji loti munthu owononga akakhala pampingo, popanda munthu omukonza? Dziko lanji loti munthu owononga akakhala pantchito, popanda munthu omuchotsa? Dziko lanji loti munthu owononga akakhala pa mulandu mukhothi, akutulukamo opanda mulandu? Dziko lanji loti anthu akhalidwe loononga akupezeka ma sector onse, mma bank, mzipembedzo, m'boma, ndi ku private sector? Ndithudi tikapanda kubwezeretsa maziko achikhalidwe chathu, palibe chomwe titaphulepo. Khalidwe lathu silingangokhala loononga zinthu. Khalidwe lathu silingangokhala lofuna kudya zinthu zaulere tisanagwirepo ntchito. Khalidwe lathu silingangokhala lolalata, lotukwana, ndi lonyoza. Khalidwe lathu silingangokhala lonamizirana mabodza ndikunenenana miseche. Khalidwe lathu silingangokhala lofuna kuti tonse tizikhala mabwana, ndiye chifukwa chosafuna kutumikirana, tizingokhalira kutcherana misampha kuti wina akangokwezedwa timugwetse. Chikhalidwe ndi maziko ofunikira pa dziko, ndiye tiyeni tiwamangenso mwachifatse.**

**Maziko ena ofunikira ndi chiyembekezo. Dziko la anthu opanda chiyembekezo silimatukuka moyenera. Ngati munthu ukadwala koma ulibe chiyembekezo choti utha**

**kuchila, kodi mankhwala umwa? Ngati munthu uli pasukulu koma ulibe chiyembekezo choti utha kumaliza, sukuluyo uzilimbikira? Ngati munthu wakumana ndimavuto pa ntchito kapena pa bizinesi, koma ulibe chiyembekezo choti utha kupeza ntchito ina kapena kuyamba bizinesi ina, upeza mphamvu zolimbikira? Ndiye ifeyo tisamayembekezere kuti tingatukule dziko popanda maziko achiyembekezo. Mzimu omanyoza chili chonse chaku Malawi, kapene kumadzitembelera tokha, kapena kumangoti ku Malawi kulibe chabwino kapena kulibe wabwino ndi mzimu ogumula maziko achiyembekezo, ndipo tisamawasekelere anthu ofuna kuchotsa chiyembekezo mmitima yathu. Popanda chiyembekezo, mlimi saafetsa mbeu. Popanda chiyembekezo, wantchito saalimbikira. Popanda chiyembekezo, olakwilana saapepesana nkumanganso ubale. Popanda chiyembekezo, anthu saasunga chuma kuti adzakolore tsiku lina. Popanda chiyembekezo, anthu saasamalira chitukuko kuti ana awo omwe sanabadwe naonso adzachipeze. Ndiye ngati tiri serious kuti tikufuna kumanganso maziko amphamvu, tiyambe kupatsana chiyembekezo, osati kugwetsana mphwayi.**

**Maziko achitatu ndi chilungamo. Dziko momwe mwachuluka chinyengo ndi mabodza zinthu sizimayenda. Tiyeni tilimbikitse kuchita zinthu mwachilungamo, osati moti ena atikonde kapena atitame. Pali zambiri zopanda chilungamo koma zoti zitha kukupangitsa kuti anthu azikuchemelera, koma zimakhala zosathandiza pachitukuko cha dziko. Ngati tili pa ntchito, tiyeni tigwire mwachilungamo. Ngati tikugulitsa malonda, tiyeni tigulitse pamtengo wachilungamo. Ngati tikumanga mseu, tiyeni timange mwachilungamo kuti usaononongeke msanga. Ngati kuli ma interview ofunsira ntchito, tiyeni tipange mwachilungamo. Ngati pali chimanga ndi feteleza ogawa, tiyeni tigawe mwachilungamo. Ngati tikupereka ripoti yazomwe zachitika, tiyeni tipereka ripoti yachilungamo. Koma vuto ndiloti mdziko muno tikumalowetsa chinyengo ndi bodza paliponse, ndiye maziko ena amene aonongeka mdziko muno ndi chilungamo.**

**Komanso powonjezera pamenepo, pakufunika maziko achinayi, omwe ndi mtendere. Akuluakulu akale anati nkhondo siimanga mudzi. Ndiye tikapitiliza mchitidwe oti tizingokhalira kukokana, kuponyerana zibakela, kumenyana ndi zikwanje, kapena kufuna kupanga ziwawa pa chiri**

**chonse chomwe tikutsutsana nacho, ndiye dzikoli zoti tili tukula tiiwale. Sizoona kuti chili chonse chikachitika, wina wathamangira ku khothi kukayambitsa mulandu, kapena wathamangira ku mseu kukayambitsa ziwawa, kapena wathamangira ku social media kukayambitsa phokoso, kapena wathamanga ndiunyolo kukamanga anthu nkuwatsekera. Ndife amodzi tiyeni tizifikirana nkukambirana mwa mtendere nkumapita kutsogolo limodzi. Mtendere wapakati pathu ndiofunika kuuteteza chifukwa pomwe palibe mtendere palibe chomwe chimatukuka.**

**Lero ndife dziko lodala kuti tikumalandira alendo amaiko ena ngati a Prezidenti aku Botswana, Advocate Duma Gideon Boko, omwe ali nafe pompano. Ndinawaitana kuti abwere tizasangalire limodzi komanso kuti azatikumbutse kufunikira koteteza mtendere wa dziko lathu. Iwowa kwawo ku Botswana kunali zisankho chaka chathachi, komwe anthu aku Botswana anawasankha kukhala Prezidenti wa dziko lawo. Koma zisankho zake zinali zotamandika chifukwa zinali za mtendere, ndipo zotsatira zake aliyense anazilandira mwa mtendere, popanda oyambitsa ziwawa kapena onyoza omwe anayendetsa zisankhozo. Mtendere otereu ndiumene tikuyenera kuumenyelera mdziko mwathu**

**muno, chifukwa mtendere ndi maziko a chitukuko komanso chuma cha dziko.**

**Let's wish each other peace on this Independence Day, and lets approach each other with peace tomorrow and the day after. I wish every one of you a Happy Independence Day.**

**As for you, my brother, Advocate Duma Gideon Boko, President of the Republic of Botswana, I thank you for accepting my invitation to come and celebrate this special day with us, and we ask you to make yourself at home here in the Warm Heart of Africa, because we do not just consider you and all the people of Botswana to be our friends. We consider you to be our brothers and sisters. And so on behalf of the Government of Malawi, I humbly request that you address us on this special day.**

**Zikomo.**